

Yehova Anathandiza Solomo Kukhala Wanzeru

1 MAFUMU 2:10-6:1; 11:1-40; 1 MBIRI 22:6-16

MFUMU DAVIDE ANALI ATAKALAMBA. IYE ANKADZIWA KUTI MWANA WAKE SOLOMO NDI AMENE ADZAKHALE MFUMU YA ISRAELI.



SOLOMO, CHONDE YENDA NANE.

INDE, BAMBO.



SOLOMO, YEHOVA AKUFUNA KUTI IWEYO UKHALE MFUMU M'MALO MWA INE.



SIZOPHWEKA KUKHALA MFUMU. YEHOVA AKUFUNA KUTI UMUMANGIRE NYUMBA YABWINO KWAMBIRI.

KOMA IMENEYI SI NTCHITO YAING'ONO UFUNIKA KUKHALA WANZERU.



BAMBO, NDINE WAMNG'ONO NDIPO SINDINGAKWANITSE KUKHALA MFUMU.

PEMPHA YEHOVA KUTI AKUPATSE NZERU NDIPO UMUMVERE. IYE AKUPATSA ZIMENE UKUFUNA.

DAVIDE ANAMWALIRA ATALAMULIRA
KWA ZAKA 40. KENAKO SOLOMO
ANAKHALA MFUMU YA ISRAELI.

SOLOMO ANAPITA KU GIBEONI
KUKAPEREKA NSEMBE KWA MULUNGU.



KUTADA, YEHOVA
ANAONEKERA KWA
SOLOMO M'MALOTO.

PEMPHA
CHIMENE
UKUFUNA KUTI
NDIKUPATSE.

CHONDE
NDIPATSENI MTIMA
WOMVERA KUTI
NDIZITHA KUWERUZA
ANTHU KOMANSO
KUSANKHA ZINTHU
MWANZERU.


SIKUTI NDIKUPATSA
NZERU NDI KUMVETSA
ZINTHU KOKHA, KOMA
NDIKUPATSANSO CHUMA
NDI ULEMERERO. NTHAWI
ZONSE UZIMVERA
MALAMULO ANGA.






SOLOMO ANAKHALA WANZERU KWAMBIRI KUPOSA MFUMU INA ILIYONSE PADZIKO LAPANSI. MOTHANDIZIDWA NDI YEHOVA, IYE . . .

ANAWERUZA MILANDU YOVUTA.



ANAMVETSA MMENE ZOMERA ZIMAKULIRA KOMANSO MMENE ZINYAMA ZIMACHITIRA ZINTHU.



ANAPEKA MIYAMBI YOKWANA 3,000.



ANACHITA MALONDA NDI AMALONDA OCHOKERA M'MAYIKO AKUTALI.

ANAMANGA NYUMBA MU YERUSALEMU
NDI M'MIZINDA YA MU ISRAELI.

ANALEMBA NYIMBO 1,005.

ANACHEREZA OLAMULIRA
OCHOKERA M'MADERA
AKUTALI AMENE ANABWERERA
KUDZAMVA NZERU ZAKE.

ANAMANGA KACHISI
WOLAMBIRIRAMO YEHOVA.

KOMA SOLOMO ANACHITA ZINTHU
MOPANDA NZERU PA NKHANI
YOFUNIKA KWAMBIRI . . .

SANAMVERE YEHOVA.

SOLOMO ANAKWATIRA AKAZI AMENE SANKATUMIKIRA YEHOVA, NDIPO ANAYAMBA KULAMBIRA MILUNGU YAWO.

ATAYAMBA KUTALIKIRANA NDI YEHOVA, SOLOMO ANAKHALA WANKHANZA.

KENAKO ANTHU ANAYAMBA KUMUPANDUKIRA.

SOLOMO ANAKHALABE MFUMU, KOMA ANAKHUMUDWITSA YEHOVA, NDIPO SOLOMO ANAKHALA WOSASANGALALA KWA MOYO WAKE WONSE.

KODI TIKUPHUNZIRA CHIYANI KUCHOKERA PA NKHANI IMENEYI?

KODI ZINATHEKA BWANJI KUTI SOLOMO AKHALE WANZERU?

KUTI MUZDIWE: WERENGANI 1 MAFUMU 3:7-9, 12.

KODI SOLOMO ANKAFUNIKA KUCHITA CHIYANI KUTI ZINTHU ZIMUYENDERE BWINO MONGA MFUMU?

KUTI MUZDIWE: WERENGANI 1 MAFUMU 3:14.

KODI N'CHIYANI CHIMENE ANTHU ONSE, NGAKHALE OMWE NDI ANZERU, AYENERA KUCHITA KUTI AKHALEDI OSANGALALA?

KUTI MUZDIWE: WERENGANI YESAYA 48:17, 18.